UMODZI

KUPYOLERA MU

UTSOGOLERI

"Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi; kuti akonzere ntchito ya utumiki kumangirira thupi la Khristu; kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiriro, ndi wa chizindikiritso cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khristu."

{Aefeso 4:8-13}

Ben Howard

UMODZI

KUPYOLERAMU

UTSOGOLERI

B e n H o w a r d

Translated To The Chichewa Language
By

Enoch Kamanula
New Testament Assembly
P.O. Box 64
Mwanza, Malawi

©2008 Ufulu wonse ndi wotetezedwa. Bukhu iri silingagulitsidwe, kapena mwa njira ili yonse kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama. Silingachulukitsidwe, kapena kutanthauziridwa mu zilankhulo zina popanda chilolezo cholembedwa kuchokera kwa:

Ben Howard
Sound Of Liberty
7286 Hwy 53W
Dawsonville, Georgia 30534 (USA)

Website Address: www.Soundofliberty.org
Email Address: TwoAnds@tds.net

Palibe mtengo pa bukhu iri, limene latheka chifukwa cha chakhumi ndi zopereka za ufulu kuchokera kwa amene Mulungu wawalankhula kuthandiza utumiki uwu. Ngati iyi iri ntchito ya Mulungu, ndiye Iye adzapereka zosowa zathu kudzera mwa anthu ake. Ambuye akudalitseni komanso akuunikireni ndi vumbulutso la Mau ake.

‘Umodzi Kupyolera mu Utsogoleri’
Uthenga wolembedwa ndi kukonzedwa kuchokera mu tepi #539
Wolalikidwa pa 31 July, 1994
Ndi Ben Howard
Dawsonville, Georgia (USA)

UMODZI KUPYOLERA MU UTSOGOLERI

Ndi
Ben Howard

Ine ndikhala ndikuwerenga ku chaputala chachinai cha Bukhu la Aefeso kuti tiyambe uthenga wathu. Ife tiwerenga malemba ochuluka pa lingaliro loti, ***"Umodzi Kupyolera mu Utsogoleri."*** Mau a Mulungu amalankhula za umodzi. Mu chilankhulo chophweka, *umodzi* ndi kukhulupirira chinthu chofanana, kuyang'ana pa chinthu chofanana, kuyenda njira yofanana, kukhala ndi lingaliro lofanana. Paulo analankhula za izo ku 1 Akorinto 1:10, *"Tiyeni tikhale ndi lingaliro lofanana ndi chiweruzo chofanana."* Mu chaputala choyamba cha Bukhu la Aroma pamene Paulo analankhula za umodzi iye anati, "*kukhala ndi chikhulupiriro chimodzi."*

Paulo analemba za mpingo kubwera ku umodzi wa chikhulupiriro. Tsopano pamene ndinena kuti, "umodzi kupyolera mu utsogoleri," Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu ali ndi utsogoleri pa dziko, utsogoleri wa utumwi, osati zokhazo, komanso ine ndikukhulupirira Iye ali ndi utsogoleri pa wina ali yense wa inu kupyolera mwa Mzimu Woyera kukutsogolerani inu panokha. Padzakhala utumiki wolalikira Mau a Mulungu pamene alaliki onse alalikira chinthu chofanana; wina sadzalalikira icho njira ina ndi wina kuchilalikira njira ina. Ine ndikulankhula za onse amene ali mwa Mkwatibwi; iwo adzazindikira chimene Mulungu akuchita ndipo iwo adzalankhula Mau njira yofanana.

Tiyeni tipemphere tisanawerenge Mau. *Atate wathu wakumwamba, mu dzina la Yesu, ife tikukuthokozani inu tsopano chifukwa cha mwai winanso kubwera ndi kudzaima pamaso panu, kukuyamikani, ndi kukuthokozani inu, Ambuye. Monga nyimbo ikunenera, "Ine sindinabwere kudzakupemphani chirichonse. Ine ndabwera kudzakuyamikani inu." Oh, Mulungu, Ine ndikupemphera kuti inu muvomereza kuyamika kwathu usiku uno, pamene tikukuyamikani inu, ife tikukulemekezani inu, ndipo ife tikuyembekezera kudzoza kwa Mulungu. Ife tikukhumbira kudzoza kwa Mulungu kuti kukhale pa ife pamene tikulankhula Mau. Mulungu ndikupemphera kuti inu mutithandiza kuchita chimene mwachiika kuti chilankhulidwe, ndi kuti muwapanga Mau awa kukhala amoyo kwa ife. Ife tinalankhula sabata yatha, Ambuye, za madzi wochapa a Mau, m'mene madzi amayendera, Mau amadzimadzi, m'mene iwo amachapira ndi kuyeretsa mpingo. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti mulora Mzimu Woyera womwewo kutidzoza ife kuti tikathe kulandira kwa inu, ndi kuti tikathe kulankhula chimene ife tikuchilandira. Ambuye, ine ndikupemphera kuti anthu adzozedwe kuti alandire chimene mupereka. Ife tikukuyamikani chifukwa cha chimenecho mu dzina la Yesu Khristu. Amen.*

Umodzi kupyolera mu utsogoleri--Yesu Khristu ndi mutu wa Mpingo; koma ine ndikufuna ndikuonetsereni m'mene Iye amabweretsera utsogoleri wake pansi ku dziko, m'mene Iye anachitira mu masiku a Baibulo, ndi m'mene Baibulo likunenera, "Yesu Khristu ali yemweyo lero, dzulo ndi kunthawi zosatha." Iye samasintha. Ine ndikufuna kuwerenga kuyamba ndi Aefeso 4:1-2- ***"Ndikudandaulirani inu tsono, ine wandende mwa Ambuye, muyende koyenera maitanidwe amene munaitanidwa nawo, ndikuonetsera kudzichepetsa konse, ndi chifatso, ndi kuonetsera chipiriro, ndi kulorerana wina ndi mnzache, mwa chikondi;"*** Tsopano ine ndikufuna inu kuti muone ichi-- "*ndikudzichepetsa konse, ndi chifatso, ndi kuonetsera chipiriro, ndi kulorerana wina ndi mnzache, mwa chikondi."* Tsopano onsewa ndi mau apamwamba pamenepo. *Kudzichepetsa* kukutanthauza kusadzikweza. Osamaganiza kuti ndiwe odziwa zonse. Osakhala opinda mayala. Kungokhala odzichepetsa pamaso pa Mulungu ndi kudalira pa Ambuye pa vumbulutso la Mau a Mulungu. Komanso akuti "*ndi kufatsa."* Mwanawankhosa ndi nyama yofatsa, ndi chimene Yesu

Khristu ali. Iye ndi Mwanawankhosa wa Mulungu, komanso Iye ndi Mkango wa Pfuko la Yuda. Pali nthawi zimene tikuyenera kusiyanitsa m'mene tingagwirire ntchito ndi m'mene tingatsogoleredwe ndi Ambuye; chifukwa Yesu anatiuza nthawi ina kuti tikhale ochenjera ngati njoka koma ofatsa ngati nkhunda. Tsopano njoka imayang'anitsitsa chimene ikufuna kuchita. Ndi ya nzeru. Iyo siimafulumira. Nthawi zambiri iyo imadikira ndipo imaonetsetsa. Khalani ochenjera ngati njoka koma ofatsa ngati nkhunda. Ndi m'mene tikuchitira mu nthawi ino. Wina akhoza kukufunsani inu funso ndipo inu simungayankhe ngakhale yankholo mukulidziwa, ngati mukuganiza kuti yankholo litsogolera ku mikangano yambiri, ndikulimbana, ndipo sizingachite bwino.

Pali chikhulupiriro chimodzi; chikhulupiriro chimenecho ndi chikhulupiriro mwa Ambuye Yesu Khristu ndi chikhulupiriro mwa Mau a Mulungu chimene Mulungu anaulura kwa atumwi ake amene anawatumiza ku m'bado wa Amitundu, monga Paulo Woyera. Palibenso malo a chikhulupiriro china! Ine ndikuuzani, Ine ndimangokonda Mau a Mulungu, ndipo ndimakonda njira za Mulungu. Inu mukhoza kudabwa chifukwa chiyani ndimakhala okondwa pang'ono nthawi zina koma sindingathe kudziletsa, chifukwa Mau awa a Mulungu ali wolondora! Ndi wodabwitsa. Ndi abwino. Nthawi zina ine ndimaganiza m'mene Mulungu amaganizira za ife Amitundu. Ayuda amatitchula ife agalu. Uthenga usanabwere kwa Amitundu ife timakhala moyo wotsika, koma Mulungu anatikonda ife Amitundu ndipo anafuna kutenga kuchokera kwa Amitundu Mkazi wa Mwana wache. Kotero anatumiza wam'thenga wapadera Paulo Woyera, kubweretsa uthenga kutiyeretsa ife ndi kutiululira ife chilungamo cha Mulungu, kutionetsera ife kuti si chilungamo chathu, koma ndi chilungamo Chake. Kotero pali uthenga wa ife, pali bukhu la ife, ndipo pali njira kuti tipeze mwangwiro chimene chifuniro cha Mulungu chiri kwa ife ndi chimene ife tikuyenera kukhulupirira.

Paulo anati, "Pali chikhulupiriro chimodzi." Kotero ngati wina anena kuti, "Kodi inu muli mu chikhulupiriro chiti?" Inde, ife tikudziwa kuti kwenikweni akunena kuti, "Kodi inu ndinu wa mpingo uti?" Mukuona, iwo afunsa mokhotetsa. Pali chikhulupiriro chimodzi chokha. Ine ndine wa *chikhulupiriro cha Mwana wa Mulungu.* Chimenecho ndiye chikhulupiriro, ndi chokhacho chimene Mulungu amachilemekeza!

Ine sindikudziwa m'mene inu mukuzimverera, koma ine ndiri okondwa kukhala pano. Ine ndiri okondwa kukuonani inu mutakhala pano. Ine ndiri okondwa kukuonani mu choonadi. Yohane anati, "Ine ndilibe chimwemwe chopambana kumva kuti ana anga akuyenda mu choonadi." Kotero, ife tikuyenda mu choonadi pano ndipo sitiri pano kuononga chimene wina wake akuchita, chifukwa tikungofuna kukhala mu chimene Mulungu akuchita. Mau a Mulungu adzawononga miyambo.

Tsopano, kodi utsogoleri ndi chiyani? Mu masiku a Paulo- Paulo anati, "Zinthu izi zimene mwandimva ndikulalikira, inu mulalikire zofanana ndi kuzipereka kwa amuna okhulupirika ena kuti alalikire zinthu izinso, kuti pakhale uthenga umodzi." Kumeneko ndi 2 Timoteo. *"Muzipereke zinthu izi kwa amuna ena okhulupirika."* Mwa kulankhula kwina, sikunali mwamalemba kololedwa pa maso pa Mulungu kulalikira china chake chosiyana ndi chimene Paulo analalikira. Iye anati ku bukhu la Agalatiya, "Ngati ine ngakhale angelo ochokera kumwamba abwera ndikulalikira chinachake chosiyana ndi ichi, akhale otembereredwa." Kotero pali njira – pali umodzi, ndipo palibe aliyense amene ali ndi ufulu wolalikira chirichonse chimene akufuna. Ife timalalikira chimene Mulungu amatitumizira ife. Mulungu amatumiza utsogoleri kupyolera mu utumiki.

Pali munthu amene analankhula kwa ine nthawi ina yake, "Chabwino ine ndiri ngati Paulo. Paulo anati, 'Ine sindinalandire ichi kuchokera kwa anthu, kapena kuphunzitsidwa ndi anthu, koma mwa Khristu Yesu yekha." Koma uku kunali kulankhula kwa udindo wa utumwi. Inu simukanatha kumumva Timoteo akulankhula zimenezo. Paulo anamuuza Timoteo, *"Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uziikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso."* (2 Timoteo 2:2) kuti wina aliyense akalankhule

zofanana. Komanso, Paulo anati, *"Koma mumangike mu mtima womwewo ndi m'chiweruzo chomwecho."* (1 Akorinto 1:10) Ndipo anati, *"Uthenga wanga,"* ku Aroma 16:25. Komanso *"Amene ndinakhala mtumiki wache, monga mwa udindo wa Mulungu umene anandipatsa ine wakuchitira inu, wakukwaniritsa mau a Mulungu."* (Akolose 1:25)

Mukuona, ndi m'mene ziriri, pamene tibwera ku mpingo timafuna kuzimverera bwino za izo. Ife timafuna kumverera ngati kuti tikulondora. Ife timafuna kumverera ngati kuti sitikungoganizira kapena kumadabwa ngati tiri olondora. Ife sitimafuna kumverera ngati kuti tataika penapake ndipo tiri opanda woyendetsa patsogolo pa bwato. Ife tikufuna kumverera tiri kunja uko kutaika pa nyanja ndipo ife mwina tikupemphera, "Ambuye, lorani bwatoli lithawire ku doko labwino penapake." Ayi. Ife sitiri mwa njira imeneyo. Si njira imene Mulungu anatisiira. Ife tikuyenda mu njira yolunjika ndipo pali utsogoleri wolunjika, ndipo pang'ono ndi pang'ono ife tikhoza kumverera bwino ndi m'mene Mulungu akutitsogolera pamene tiziona kupyolera mu maso mwa Mzimu Woyera. Ine ndikukhulupirira kuti ndizofunika, chifukwa Mulungu amalankhula za kulowa mu mpumulo umenewo. Kodi tingalowe bwanji mu mpumulo mwa Ambuye ndi kukhala bwinobwino pokhapokha titamverera ndi kudziwa ndi kuona mwa vumbulutso peni peni pamene ife tiri ndi m'mene Mulungu akutisunthira? ***Umodzi kupyolera mu utsogoleri--*** Muli utsogoleri mu thupi la Khristu. Amen.

Kupitiriza ndi lemba. Vesi 5-7- ***"Ambuye m'modzi, chikhulupiriro chimodzi, ubatizo umodzi, Mulungu m'modzi ndi Atate wa onse, mwa onse, ndi mkati mwa onse.*** (Ine ndikuzikonda zimenezo) ***Ndipo kwa yense wa ife kwapatsidwa chisomo, monga mwa muyeso wa mphatso ya Khristu."*** Zikutanthauza kuti ngati Mulungu wakupatsani inu mphatso, Iye amakupatsani inu chisomo kuyendera palimodzi ndi mphatso imeneyo. Izi, makamaka, zikukamba za mphatso zotumikira. Ngati Mulungu amuitana munthu kulalikira, Iye adzamupatsa iye chisomo; ndipo pamene akupatsani inu chisomo, Iye adzakupatsani inu mzeru yakuchita zinthu izi. Mvetserani pamene tikupitiriza.

Vesi 8- ***"Chifukwa chake anena, Mmene anakwera kumwamba, anamanga ndende undende, naninkha za ufulu kwa anthu."*** Tsopano Iye akulankhula za mphatso zotumikira apa. Iye sakulankula za mphatso zisanu ndi zinai za mpingo. Iye anapereka mphatso *zotumikira* izi kwa amuna, ndiye kotero, mkazi sangakhale mtumiki wa uthenga mpakana kumalalikira Mau a Mulungu. Utsogoleri uli mwa mamuna. Chifukwa chiyani? Chifukwa mamuna akhoza kupanga lingaliro ndi kuima nalo bwino. Ngati lamulo la ponseponse, akazi akhoza kusunthika ndi zokhumba nthawi zambiri, (iwo ali ndi chikhalidwe china, mukuona.) ndipo pamene inu mukuchita ndi Mau a Mulungu nthawi zina inu simungasinthe. Inu simungasunthike ndi zokhumba. Inu mukungoyenera kuima moona ndi ku Mau amenewo ndi kulora zinazo kugwa pamene zingagwe. Kuyambira m'munda mwa Edeni, Mulungu anaika utsogoleri mwa mamuna, kotero kuti pamene anakwera kumwamba Iye anamanga ndende undende koma Iye anasiya mphatso apa, mphatso zotumikira, kwa amuna. Pamene Yesu anaitana atumwi khumi ndi awiri, iye sanaitane mkazi ngakhale m'modzi kukhala mtumwi. Palibe mkazi ngakhale m'modzi mu Baibulo amene Mulungu anamuitana kukhala mulaliki. Iye anapereka mphatso izi kwa anthu, ndipo muli umodzi mu utsogoleri. Mukuona, utsogoleri. Ngati muthu ayesera kulalikira uthenga, inu mukudziwa iye ali kunja kwa chifuniro cha Mulungu, inu mukudziwa iye ali kunja kwa Mau a Mulungu, ndipo inu mukudziwa kuti izi sizingakhale monga mwa Mau a Mulungu. Mau a Mulungu ndi amene ali wolondora. Mulungu anati, "Mau anga akhale woona ndipo mau a munthu ali yense akhale abodza," (aliyense amene azilankhula mosiyana.)

Kotero akupitiriza apa, vesi 9-10 akuti- ***"(Koma chakuti, Anakwera, nchiyani nanga koma kuti anatsikiranso ku Madera a kunsi kwa dziko?*** (Kunali kuti abweretse oyeramtima aku Chipangano Chakale) ***Iye wotsikayo ndiye yemweyonso anakwera, popitiriratu miyamba yonse, kuti akadzaze zinthu zonse.)"*** Tsopano taonani, pamene Iye anakwera

kumwamba Iye anachita china chake, mukuona. Iye anachita chinachake. Mphatso zotumikira zomwe zinali mwa Iye, Iye anazisiya izo pa dziko. Taonani chimene Iye anachita; Vesi 11 akuti, ***"Ndipo anapatsa ena akhale atumwi…"*** Apa ndi pamene utsogoleri wanu ukuyamba mu utumiki. Ndi angati amene amva chimene ndalankhula? Ndi pamene utsogoleri wanu ukuyamba mu utumiki. Ndi kupyolera mu udindo wa utumwi, monga m'mene Paulo anali mtumwi kwa amitundu mu mpingo woyamba ndi utsogoleri monga mwa kayendedwe ka chiphunzitso cha mpingo. Chinayamba koyamba kupyolera mwa Paulo ndi kutsikira kwa ena a mu utumiki, mpakana kumapeto kwake onse amalankhula chinthu chimodzi.

Kotero iye anati, Aefeso 4:11- ***"Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi;"*** Tsopano Iye anawapatsiranji? Vesi 12- ***"Kufikitsa oyera mtima ku ungwiro,"*** (kufikitsa oyera mtima ku ukulu msinkhu). Pali lemba ku bukhu la Ahebri limene likuti, "Mwana amakhumba mkaka wa Mau, koma chakudya cholimba ndi cha iwo amene ndi okula msinkhu." Tsopano kukula msinkhu ndi kukhala wangwiro, kukhwima, ndi kufika kumapeto. Ine ndikukhulupirira kuti pali chakudya cholimba chimene chikuperekedwa ku mpingo, chifukwa mpingo wafika pokula msinkhu. Ine ndikukhulupirira kuti alipo ena amene akukhoza kudya chakudya cholimba ichi ndipo pali utsogoleri lero pa dziko kupyolera mu utumiki wa utumwi, ndipo pali atumwi. Inu mukuti, "Ali kuti m'bale Howard?" Mulungu adzazindikiritsa yense wa iwo ndi utumiki umene ali nawo. Osati ndi kulakwa mtumwi kunena kuti "Umenewo ndi udindo wanga. Ndi chimene Mulungu wandiitanira." Sikulakwa konse, koma si china chake chimene iye adzakhala akunyadira. Ndi chinachake chimene anthu adzaona ndi kudziwa, ndiponso kupyolera mu uthenga wake umene iye adzalalikira zidzabweretsa Mpingo ku umodzi wa chiphunzitso. Amen.

Chabwino, akuti apa mu vesi 12 ndi 13 kuti utumiki usanu waperekedwa kufikitsa oyeramtima ku ungwiro, ***"...ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu: kufikira ife tonse tikafike ku umodzi wa chikhulupiriro…"*** Apo pali mau anu oti umodzi kenanso- umodzi kupyolera mu utsogoleri. Mukuona, utumiki usanu waperekedwa kufikitsa oyeramtima ku ungwiro, ku ntchito ya utumiki, ndi kumangirira thupi la Khristu, mpaka titafika tonse ku umodzi wa chikhulupiriro. Kotero utumiki umabweretsa umodzi, sichoncho? Ndipo sitingakhale ndi umodzi pokha pokha titazindikira utumiki. Kodi mukudziwa chifukwa chake? Chifukwa aliyense wa inu ali ndi mutu pa mapewa ake ndipo ali yense wa inu ali ndi malingaliro, bongo, mkati mwa mutu wake. Ali yense wa inu akhoza kuganiza; ndipo aliyense wa inu amaganiza. Nthawi zambiri timaganiza izi, ndi kuganiza izo, koma nthawi ina ndinamumvapo M'bale Branham akuti, "Ife tiribe "*kusaganiza*" tikafika ku zinthu zimene Mulungu analankhula. Ndi Mau a Mulungu amene ndi olondora." Pamene tilankhula za malingaliro anu, tikulankhula za chinthu chotuwa kuti kupyolera mu njira ya chozizwa (ndi Mulungu yekha amene akudziwa m'mene zimakhalalira) malingaliro ndi zoganiza m'mene zimadutsira. Koma Mulungu anaika mu Mau chinachake kuti tikathe kudziwa—ngati malire kapena chinachake. Iye anaika m'menemo (mu Mau olembedwa) kuti *Iye anaika mu mpingo choyamba atumwi,* kotero pamene tipeza chidziwitso kapena vumbulutso, kapena chinachake cha mtundu umenewo, tapeza chinachake choti tikhoza kuyezera kuti tione ngati chiri cholondolora. Paulo anati "Ine ndikangochoka padzadzuka amuna kulankhula zinthu zosiyana kuti adzipezere ophunzira a iwo okha." Ndipo chimenecho chinali kudzala mbewu ya Chinikolai. Aliyense anapita njira yake, chifukwa amafuna kumanga chinachake kwa iwo okha. Koma ife tikufuna kumanga chinachake cha Yesu Khristu! Ife tikufuna kuona mpingo utafika ku ungwiro mwa Yesu Khristu! Iye ndi mutu wa mpingo; ndipo Mulungu anaika mu mpingo choyamba atumwi. Ine ndikulankhula za utsogoleri. Apo ndi pamene utsogoleri ukuchokera. Ndipo zikulankhula momveka bwino apa (Aefeso 4:11-12) kuti Iye anapereka utumiki uwu usanu ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu, kufikira tonse tifike ku umodzi. Monga mutu wanga ukulankhula, "Umodzi kupyolera mu Utsogoleri."

Inu mukhoza kunena, “Chabwino, ine ndiri ndi Mzimu Woyera, M’bale Howard.” Ngati inu muli ndi Mzimu Woyera ndipo Mzimu Woyera ukukutsogolerani inu, sudzakutsogolerani inu mosiyana ndi Mau. Iwo udzakutsogolerani inu mu matsamba a Mau a Mulungu, chifukwa Paulo anati, “Ine ndaika maziko,” ndipo anati, “Palibenso maziko ena amene angaikidwe.” Iye sanalankhule kuti sitingathe kumanga nyumba, koma anati simungathe kuika maziko ena. Ife sitingathe kuchoka pa chimene Paulo analankhula ngati maziko a chiphunzitso. Iye anati, “Ine ndakupalitsani ubwenzi (kapena kukudziwitsani kwa inu) kwa Khristu.” Iye anakwatitsa ife. Pali ukwati woti uchitike mu nthawi ino yotsiriza. Ukwati umenewo ndi pamene Khristu ndi Mkwatibwi akukwatirana. Zidzachitika kupyolera mu umodzi wa utumiki; utumiki kubweretsa umodzi wa chiphunzitso, wa lingaliro, wa zolinga, ndi ntchito pamene Khristu akuchita kudutsa mu izo. Inu mukuti, “Kodi Khristu adzachita kupyola mu izo?” Kodi ndinalankhula chiyani chokhudza Mau a Mulungu poyambira? Bukhu ndi lorondora, Bukhu ndi loona, ndipo chirichonse Bukhu lilankhula, ndi m’mene zidzakhalire. Kaya ine ndikuganiza kuti zikhale mosiyana kapena inu mukugaiza kuti zikhale mosiyana, zikhala m’mene Bukhu likuti zidzakhalira. Ndipo Bukhu apa likuti Iye adzabweretsa mpingo ku umodzi kupyolera mu utumiki usanu.

Ndiye kenako tikutenga vesi 13- ***“Kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiriro, ndi wa chizindikiritso cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khristu.”*** Tsopano, abale ndi alongo, izi zikutibweretsa ife ku malo ena mwa Iye. Kodi timafika bwanji ku umodzi umenewo? Timafika bwanji ku malo amenewo? Umodzi kupyolera mu utsogoleri--mukuona, utsogoleri wa Mzimu Woyera, utsogoleri mu utumiki. Tsopano anthu ena amati, “Ine ndipemphera ndi kutenga wanga kupyolera mwa Mzimu Woyera.” Ngati mutatero, ndipo Mzimu Woyera ndikulankhula ndi inu, kodi mukudziwa chimene Mzimu Woyera adzachita? Mzimu Woyera udzakulozerani inu ku Mau; Iwo udzakulozerani inu ku utumiki weniweni wa moyo mu nthawi ino. Mzimu Woyera udzachita monga mkazi uja wa pa chitsime anachitira. Pamene iye analowa m’mudzi anati, “Bwerani, mverani munthu amene wandiuza ine chirichonse chimene ndinachita. Ameneyi kodi si Khristu? Bwerani mudzaone munthu amene wandiuza chirichonse!” Mwa kulankhula kwina, Mzimu Woyera udzakulozerani inu kwa winawake amene ali mu Mau a Mulungu, winawake amene akulalikira Mau a Mulungu; chifukwa Mulungu anasankha mwa kupusa kwa kulalikira kupulumutsa iwo amene akhulupirira. Ndi mwa kulalikira Mau a Mulungu; ndi chimene Mzimu Woyera udzakuphunzitsani inu. Inu mukuti, “Chabwino, M’bale Howard, Ine ndimaganiza Iye akhoza kundipanga ine kupfuula. Ine ndimaganiza akhoza kundipatsa ine maloto.” Iye adzatero. Iye adzakupatsani inu maloto. Iye adzakupatsani inu masomphenya. Iye adzakupatsani inu masomphenya. Iye adzakupangani inu kupfuula. Iye adzaika chimwemwe mu moyo wanu. Iye adzakupatsani inu mphatso ya malilime. Iye akhoza kuchita zinthu zonsezi. Koma ikafika nthawi yoti inu mukhulupirire chinachake chokhudza Mau a Mulungu, Iye sadzasintha Mau ake kwa inu. Iye adzakulozerani inu molondora ku Bukhu, ndipo Iye adzalankhula chimodzimodzi m’mene ine ndikulankhulira usiku uno- kuti Iye ali ndi utumiki umene ukulalikira Mau a Mulungu.., Iye ali ndi utsogoleri wa utumwi ndipo ali ndi abusa ndi aphunzitsi amene akulalikira ndi kuphunzitsa Mau woona a Mulungu. Iye sadzachita mosiyana ndi zimenezo. M’bale ndi mlongo, ine ndikudziwa kuti ndi chakudya cholimba, koma iwo okula msinkhu akhoza kudya chakudya cholimba. Ndi m’mene Mulungu angazichitire.

Mu zinthu izi zimene Mulungu akuchita, iye akutisiya ife opanda chowiringula. Ine ndikukhulupirira ziri mu chaputala chachiwiri cha Bukhu la Aroma kumene akuti tidzakhala opanda chowiringula. Mukuona, Mulungu kuzipanga izo zomveka. Iye akuziika poyera apa. Iye ali nawo amuna amene anawaika, amene wawadzoza, amene Iye anawadzutsa, ndipo sikuchitachita kwathu; ndipo sintchito yathu pa amene angamugwiritse ntchito. Iwo amene adzawagwiritsa ntchito sadzakhala akumapita ndikumaimba lipenga nthawi zonse.

Zidzachitika mophweka. Chinthu china, pamene zichitika, zidzakulozerani inu ku Mau ndipo zidzakuikani inu molimba ku Mau a Mulungu mpaka simungathe kuzifunsa izo.

Paulo anati, “Ine ndikapita amuna ena adzadzuka…” Pamene mibado ya mpingo imayamba iwo anali atachoka kale, ndipo tirigu ndi nansongole zimakulira palimodzi. Yohane anati mu 96A.D. “Iwe wagwa;” ndipo mpingo unakhala mu chikhalidwe chake chakugwa mpakana nthawi yakumapeto. Koma Mulungu anati, “Ine ndidzaubwezeretsa.” Ndipo pamene Iye adzatero, Iye adzabwezeretsa mu utumiki womwewo umene mpingo woyamba unali, maudindo womwewo, osati anthu womwewo, maudindo womwewo, ndiye kukhala atumwi, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi. Pali atumwi lero poyera ndipo akuima pamenepo ndi kunena, **“Njira ndi iyi. Yendani m’menemo.”** Koma ambiri akuti, “Ayi, imeneyo si njira imene *ine ndikuganiza* kuti ingakhale.” Mukuona, pamenepo ndi pamene pakubwera vuto. “Mukuona, ngati mutapemphera ndi kufunsira Mulungu, Iye adzakulozerani inu ku utumiki. Iye anachita njira yonse kudutsa mu Baibulo.

Monga m’dindo uja ku Machitidwe, chaputala 8, pamene Filipo anayandikira yekha ku galeta, apo panali m’dindo, akuwerenga Mau a Mulungu. Apo anali, Mulungu kuchita ndi mtima wake. Iye anali ku Yerusalemu ku chitsitsimutso chachikulu ndipo amawerenga m’menemo pamene akuti ku Yesaya, *“Ngati nkhosa anatengedwa kukaphedwa, ndi monga mwana wa nkhosa ali du pamaso pa womsenga, kotero sanatsegula pakamwa pache. Iye anaphedwa”* Ndipo Mzimu wa Mulungu unalankhula ndi Filipo ndi kuti, “Pita yandikira kwa m’dindo.” Filipo anatero. Ndipo Filipo anati kwa m’dindo, “Kodi muzindikira chimene muwerenga?” Kodi mukudziwa chimene chinali yankho? Mdindo anayankha nati, “Ndingathe bwanji popanda munthu wonditsogolera?” Ife tikhoza kunena kuti, “Kodi Mzimu Woyera sungathe kufotokoza icho?” Mzimu Woyera ukanatha kuchita chirichonse ukufuna, koma Mulungu ali ndi njira zimene ali nazo zimene amagwiritsa ntchito ndipo samapita kunja kwa zimenezo pa chirichonse. Pakhoza kukhala malo ena kutali ku thengo kapena china chake kumene utumiki sukugwira ntchito ndipo Mulungu adzachita chimene akufuna kuchita kumeneko. Koma Iye adzakhala ndi Mkwatibwi.

Mu masiku a Paulo, Paulo anali mtimwi. Mu masiku a Baibulo kunali aneneri, aneneri a ku Chipangano Chatsopano monga Yuda, Sila, Agabo, aneneri amenewa anali m’menemo, Mulungu amamangirira utumiki umenewo. Koma mukuona, Mulungu amadziwa kuti zidzagwa. Iye amadziwa kuti sizidzafika ku ungwiro kumeneko. Ndipo mu Bukhu la Genesis, Adamu ndi Hava, iwo asanafike ku ungwiro, kunabwera kugwa. Koma Mulungu anazibwezeretsa, kupyolera mwa munthu wachiwiri, Khristu, Iye anayamba chilengedwe chatsopano. Pamene anati, “Kwatha,” pa mtanda, chilengedwe choyamba chinatha ndipo Iye anayamba chilengedwe chatsopano pa tsiku la Pentekosite. Chilengedwe chatsopano ichi chiri ndi utsogoleri watsopano! Ine ndikumverera kudzoza kumeneko; alemekezeke Ambuye! Ndipo pamene izi zichitika… Mvetserani Baibulo; musangotenga mau anga pa izo, mvetserani Baibulo. Ndikanakhumba ndikanazilankhula monga ndikuzimverera. Baibulo iri ndi choonadi! Baibulo iri ndi lolondora. Mau awa a Mulungu sangalephere. Palibe ngakhale lonjezo limodzi la Bukhu limene lidzapita.

Pakulankhula izo, ndiloreni ndiwerenge vesi 14. Tikatha kubwezeretsedwa ku umodzi wa Mzimu mwa utsogoleri wa utumiki usanu, taonani chimene Aefeso 4: 14 akunena. Akuti, ***“Kuti tisakhalenso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengeka tengeka ndi mphepo yonse ya chiphunzitso, ndi tsenga la anthu, ndi kuchenjerera kutsata chinyengo cha kusocheretsa.”*** Tsopano chimene akulankhula apa ndi ichi: Pamene utumiki uwu udzazindikirika, ife sitingathenso kugwedezeka gwedezeka ndi kutengeka ndi mphepo iliyonse ya chiphunzitso. Padzakhala ziphunzitso zosiyanasiyana uko, koma ife tamva uthenga, tiri ndi utumiki, ife tiri ndi utsogoleri wa Mulungu, ndipo sitingathe kugwedezeka gwedezeka uku ndi uko! Ine sindikudziwa ngati inu mukuyamikira zimenezo kapena ayi, akuluakulu, koma mukuyenera kutero. Pamene mutuluka kunja ku dziko uko ambiri

osiyanasiyana akuti, “Ife timazikhulupirira mu njira iyi. Zikhoza kukhala njira imeneyo. Ndi zotheka ziri mu njira iyi. Kodi yankho ili pati?” Mulungu ali nalo yankho. Inu mutenga Sabata la 70 la Danieli mwa chitsanzo, anthu ambiri amati, “chabwino, likhoza kukhala zaka zitatu ndi theka kapena zaka zisanu ndi ziwiri; ife kweni kweni sitikudziwa, komabe sizichita kanthu kali konse.” Inu simumazitenga zimenezo kuchokera ku Mau a Mulungu!

Pamene utumiki uwu udzazindikirika; Paulo anati, “Ife sitidzagwedezeka uku ndi uko?” Kodi mungathe kukhulupirira izo? Kodi mukukhulupirira kuti sitidzagwedezeka uku ndi uko? Ife sitidzadabwa chimene tidzakhulupirira ndi chimene sitidzakhulupirira. Inu mukuti, “Chabwino, Ine sindikudziwa, Mlaliki. Aliyense ali ndi ufulu wokhulupirira chimene akufuna.” Inde muli nawo; koma ngati muli mwana wa Mulungu, inu mumapereka maufulu anu ku njira za Mulungu. Nkhosa ili ndi ufulu pa ubweya wake, koma umapereka kwathunthu m’manja mwa ometa bweya ndipo umadalitsa iwo ozungulira iyo ndi ubweya wake. Kotero ife tiri ndi ufulu, inde, ngati aliyense payekha payekha kukhulupirira chimene tikufuna. Koma chinthucho ndi ichi…, *“kufuna kwanu”* kudzasinthidwa. Chinthu chimodzi chimene inu mudzafuna kukhulupirira ndi kulondora kwa Mau a Mulungu. Palibe chimene chidzakwanira. Inu simudzakhala okondwa ndi chiri chonse. Ndipo pamene inu mupereka maufulu anu kwa njira za Mulungu Paulo anati ku Bukhu la Ahebri, “Ife timalowa mu mpumulo.” Ife sitikuyenera kuvutika ndi kumadandaula za zinthu zimenezo.

Ine ndikungomuyamika Mulungu chifukwa cha madalitso Ake, chifukwa cha m’mene Iye watsegulira kwa ife Bukhu la Chivumbulutso (limene tinasindikiza ndi kulitcha “Bukhu lomasuliridwa la Chivumbulutso,” limene liripo kwa inu ngati mutalifunsa). Ine ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha kudziwa zisindikizo zisanu ndi ziwiri, mibado ya mpingo isanu ndi iwiri, ndi m’mene amithenga asanu ndi awiri anabwerera. Ine ndimakonda kuwerenga za Khristu m’mene Iye amayenda pakati pa zoikapo nyali zisanu ndi ziwiri, ndipo ndinalibe lingaliro la chimene zimatanthauza. Ine ndinalibe lingaliro la chimene nyenyezi zisanu ndi ziwiri zinali. Ine ndinalibe lingaliro la chimene mizimu isanu ndi iwiri imatanthauza. Ine ndinalibe lingaliro la m’mene chilemba cha chilombo chidzachitikire, kapena za aneneri awiri ku Israeli amene adzakantha dziko lapansi ndi kusandutsa madzi kukhala magazi. Ine ndinalibe lingaliro la zimenezo. Ine ndikukuuzani akuluakulu, ife tadalitsidwa moti sitingathe kufotokoza. Ife tadalitsidwa kwakukulu mu njira yopambana. Nthawi zina ine ndikuganiza timapeza chakudya chambiri mpaka timalephera kuzindikira madalitso athu. Ine ndiri ndi zithunzi zimene zinajambulidwa ku Philippines ndipo ambiri akukhala mu nyumba za udzu zazing’ono. Ngati atati apeza mbale imodzi ya mpunga pa tsiku ndi kudya iwo amadziyesa okha anthu amwai kwambiri. Iwo alibe magetsi kapena madzi ku malo akunja uko; komabe, kuli anthu amene amakhala kumeneko ndiwo anthu okhulupirira Mulungu. Ena mwa ana a Mulungu aliko komweko. Mukuona, ife ndife odala, akuluakulu! Ife ndi odala, ndife odala, ndife odala, ndife odala! Tadalitsidwa mwa Mzimu Woyera. Tadalitsidwa mwa Yesu Khristu potitumizira ife utumiki kuika malingaliro athu molunjika, kutipatsa ife mtendere wa mumtima pa chimene tikuchikhulupirira ndi kumene tikupita. Ine ndikukhulupirira zonsezi ndi zokhazikika kwa anthu a Mulungu pa chimene utumiki wa utumwi uli ndi kumene utsogoleri uli. Mukuona, umodzi kupyolera mu utsogoleri.

Kenako akupitirira apa--*kuti tisakhalenso ogwedezeka gwedezeka uku ndi uko*. Apa pali chimene utumiki udzachita, vesi 15- ***“Koma ndi kuchita zoona mwa chikondi tikakule m’zinthu zonse, kufikira Iye amene ali mutu ndiye Khristu:”*** Pamene ichi chiyamba kuchitika thupi lidzayamba kumangirizana wina ndi mzache. Mukuona, ena akhoza kuimba, ena kuchitira umboni, ena kuimba zida, ndi zina zotero. Mukuona, aliyense kuyenda mu njira yake ndi kudalitsa wina ndi mzache. Inu simumayembekezera mlaliki akuuzeni chochita nthawi zonse. Nthawi zina mpingo ku South Carolina udzayamba kuimba ndi kupembedza

Mulungu ife ngakhale tisanafike. Zimatanthauza zambiri kwa ine kuona anthu akusuntha ndi kuyamba kupembedza Mulungu mu Mzimu ndi choonadi.

Apa pali chimene akulankhula mu vesi lotsatirali. Vesi 16- ***"Kuchokera kwa Iye thupi lonse, lokowanidwa ndi lolumikizidwa pamodzi…,*** Tsopano sakulankhula za utumiki. Ine ndikufuna inu muone ichi. Zikuyambira uko ku vesi 8 kulankhula za chimene Khristu anachita pamene Iye anakwera kumwamba--Iye anatsanulira mphatso zotumikira koyamba, mukuona, mphatso zotumikira izi, ndipo mphatso izi zidzabweretsa Mpingo ku umodzi komanso kukulamsinkhu. Kenako akatero sadzagwedezekanso uku ndi uko ndi kutengeka ndi mphepo iliyonse ya chiphunzitso. Koma vesi 16 ikuonetsa mpingo wonse, thupi lonse, ndi wina aliyense akugwira ntchito pamenepo, mukuona. Ine ndikukhulupirira mukuona zimenezo. Aliyense akuchita mbali yake- membala aliyense.

Tiyeni tiwerenge chimenecho. Vesi 16- ***"Kuchokera kwa Iye thupi lonse, lokowanidwa ndi lolumikizidwa pamodzi pothandizanapo mfundo yonse, monga mwa kuchititsa kwa chiwalo chonse pa muyeso wache, lichita makulidwe a thupi, kufikira chimango chache mwa chikondi."*** Izi zikutanthauza kuti thupi lonse likulowamo, osati mlaliki yekha, osati utumuki okhanso, koma thupi lonse likuyamba kudalitsa wina ndi mzake, kuyamba kugawirana zosowa za wina ndi mzache. Mu msonkhano mudzaona ulemerero wa Mulungu kuwalira oyeramtima ndi mphatso za Mzimu ndi aliyense kugwiritsa ntchito mphatso yache, mphatso ya malirime, mphatso yoimba, mphatso yonenera, ndi zina zotero. Mukuona, pamene utumiki utenga malingaliro ndi kuganiza kwa anthu pamodzi, kuyenda mu njira yolondora mwachiphunzitso, kenako zimamasula malingaliro anu kudzipereka kwa Mulungu, kupembedza Mulungu, kulora Mulungu kukugwiritsani inu ntchito, kunenera, kulankhula malirime, kuimba, kumangirira. Ndi pamene oyeramtima atenga china chake kuchokera kwa Mulungu. Limenelo ndilo dongosolo la mpingo pamenepo.

Umodzi wa Mzimu wabweretsedwa, chifukwa pali utumiki. Kenako mpingo ukubweretsedwa ku umodzi wa chikhulupiriro. Kenako mpingo sukugwedezekanso uku ndi uko. Chimachitika ndi chiyani pamene chimenecho chichitika? Ife timakula mwa Iye. Kenako pfupa lirilonse, memembala aliyense wa thupi, amayamba kudalitsa mzache. Aliyense amapeza malo ake. Mulungu akhoza kuika nyimbo mu mtima wa wina aliyense mu msonkhano ndipo iwo adzakhala pansi mwina ndi kumangolowa mu nyimbo, chifukwa iwo sangadandaule ngati ziri zolondora kapena icho ndi cholondora. Iwo sangakhale ali apo ndi malingaliro awo osweka ndikumaganiza, "Ine sindikudziwa ngati izi ziri zolondora kapena ayi. Ine sindikudziwa ngati mlaliki uyu ali wolondora kapena ayi." Ayi, kupyolera mu utsogoleri wa Mulungu Iye wazibweretsa ku umodzi. Kupyolera mu utumiki wake weniweni umene mukuuona umene Iye waika mu mpingo, Mulungu waziika ndi kuzichita kwa inu. Koma tsopano ino ndi nthawi yanu kuyamba kudzipereka inu nokha ku Mzimu Woyera, kudzipereka nokha kwa Mulungu, ndi kudzipereka nokha ku mphatso zimene Mulungu anaziika mwa inu. Inu simukuyenera kukhala pamenepo ndi malingaliro anu osautsika-"Kodi pali m'modzi mu umulungu kapena alipo atatu?" "Kodi ine ndibatizidwe mu dzina la Yesu Khristu kapena la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera?" "Kodi mlaliki uyu akulondora kapena uyo akulondora?" "Kodi ndichite chiyani apa?" "Ndingazikhulupirire bwanji izi?" Ayi; zonse izo zidzapita; ndipo zonse izi zapita kwa iwo onse amene akuzindikira utumiki wa Mulungu ndi chimene Mulungu akuchita mu tsiku ili ndi nthawi iyi.

Kenako pakubwera pa malo mphatso zisanu ndi zinai. Pali magulu atatu, mphatso zitatu gulu lirilonse. Pali mphatso zitatu zamphamvu, zitatu za mavumbulutso, zitatu za mau. Pamene Mulungu akhazikitsa utumiki (kubweretsa poyera, kuika maziko olimba, ndikuupanga kudziwika) kufika ku vesi 16, kenako timayamba kumangirirana wina ndi mzache ndi mphatso zimenezi zimene Mulungu amatipatsa ife. (1 Akorinto 12) Inu mukuyenera kukhala ndi mphatso zimenezi. Pamene mukhala okhazikika pa chiphunzitso chanu, ndipo inu mukudziwa chimene mwakhulupirira, ndipo tonse tiri mu umodzi, ndiye inu

mukhoza kudzipereka nokha kwa Mulungu ndipo mphatso izi zidzayamba kugwira ntchito pakati pathu.

Chabwino, kodi mphatso za mau zimenezi ndi ziti mu Baibulo? Malirime, kumasulira, ndi uneneri. Kenako pali mphatso za mavumbulutso zitatu, pamene Mulungu akupatsani inu vumbulutso. Mphatso za mavumbulutso izi ndi mavumbulutso apamwamba amene amachokera kwa Mulungu kubwera kwa inu. Awa ndi mau a chidziwitso, mau a mzeru, ndi kuzindikira mizimu. Mau a chidziwitso ndi chidziwitso chapamwamba. Mau a mzeru ndi pamene inu mudziwa choyenera kuchita, zinangobwera kwa inu ndipo mosachedwa inu mumadziwa kuti zochitika, ndipo inu munazichita, ndipo chinali chinthu cholondora kuchichita. Mwakuzindikira mizimu inu mudzadziwa kuti ndi mzimu wanji umene ukukukokani inu. Mulungu adzakulorani inu kuzindikira mzimu umenewo ndikudziwa ngati uli wa Mulungu kapena ayi.

Kenako pali mphatso zitatu za mphamvu zopereka mphamvu ku mpingo. Chikhulupiriro chimodzi. Mwa chikhulupiriro inu ndinu okhoza kugonjetsa. Mwa chikhulupiriro inu ndi okhoza kupita kuchokera ku chigonjetso kupita ku chigonjetso. Inu ndinu okhoza kuchiritsidwa. Mphatso ya chikhulupiriro imeneyo ili monga chonchi: inu muli ndi chikhulupiriro, inu mumakhulupirira Mulungu. Ziri ngati m’mene zinaliri Paulo atalumidwa ndi njoka. Paulo amatenga nkhuni ndi kumakoleza moto, ndipo chinjoka cha chiphe chinamulumphira iye ndikumuluma. Iye akanatha kutupa ndi kufa pomwepo, koma Baibulo likuti, “Paulo anangochisasa ndipo sanamve ululu.” Mukuona, iye sanachiritsidwe, chifukwa sanadwale. Chinali chiyani, iye anali ndi chikhulupiriro. Mukuona, Mulungu anamuuza iye, “Monga wandichitira umboni ine ku Yerusalemu, ukandichitiranso umboni ku Roma.” Iye amadziwa amapita ku Roma, kotero mwa chikhulupiriro iye sanamve kupweteka. Kotero, imodzi mwa mphatso zitatu za mphamvu ndi chikhulupiriro.

Ina ndi kuchita zozizwa. Mukuona, pali mphatso yochita zozizwa. Kodi chozizwa ndi chiyani? Chozizwa si kwenikweni machiritso, ngakhale chikhoza kukhala chozizwa. Chozizwa chiri ngati pamene Paulo amalalikira uthenga ndipo iye anati anazindikira munthu amene anali ndi chikhulupiriro amene anali opunduka kuchokera m’mimba mwa mai wake, ndipo analankhula Mau nati, “Dzuka pa mapazi ako,” ndipo munthuyo anadzuka ndi kuyamba kuyenda. Chimenecho ndi chozizwa. Ndi machiritso, komanso ndi chozizwa.

Ndiloreni ndipereke kufotokoza kwina kwa chozizwa. Ine ndikukhulupirira kuti ndi ku Machitidwe chaputala 9. Dolika anali atamwalira. Anali atamutengera iye mu chipinda chapamwamba ndipo amalankhula zabwino zonse zimene iye anachita. Ndipo anamva kuti Petro anali ku Yoppa, kotero anatuma uthenga kuti Petro abwere; osati kuti adzalalikire pa maliro, koma amayembekezera Mulungu kuchita chozizwa. Kotero Petro anabwera. Iwo amalira, ndipo Petro anawatulutsa kunja. Iwo anayang’ana pa mkazi uyu; iye samasowa machiritso. Machiritso sakanamuthandiza iye. Iye anali atadutsa kale gawo limenelo. Iye anayang’ana pa mkazi uyu ndi kunena, “Dolika;” (Iye analankhula ndi mkazi wakufa.) ndipo Baibulo likuti iye anatsegula maso ake, ndipo pamene anaona kuti anali Petro iye anadzuka. M’bale, chimenecho ndicho chozizwa. Monga m’mene Yesu anamuitanira Lazaro kuchokera ku manda; chimenecho ndi chozizwa. Mukuona, mphatso izi ziri mu mpingo, ndipo tikuyenera kudalitsidwa nazo. Ife tikuyenera kumangirira wina ndi mzache ndi izo. Ndipo pamene tibweretsedwa mu umodzi kupyolera mu utumiki, ndipo zina zonse zimapeza malo ake, ndipo zikhoza kukumasulani inu ku kusautsika kwa kudandaula za kuti mukulondora kapena ayi mu chikhulupiriro chanu, chifukwa inu mudzadziwa kwathunthu.

Izi ndi ziwiri za mphatso za mphamvu (chikhulupiriro ndi kuchita zozizwa). Palinso ina. Imeneyi ndi machiritso; kumene Mulungu mwantheradi amakuchiritsani inu. Panali anthu mu masiku a Baibulo amene anali ndi *mphatso* za machiritso kumene amangotha kupempherera anthu ndipo iwo amachiritsidwa. Si yense amene ali ndi *mphatso* ya machiritso. Ife tikhoza kukhala ndi chikhulupiriro, ndi kukhulupirira, ndipo Mulungu akhoza kuchiritsa; koma anthu

ena ali ndi mphatso ya machiritso. Iwo akhoza kuika manja pa anthu, kuwapempherera iwo, ndipo zimaoneka ngati Ambuye amangosuntha makamaka kupyolera mwa mu munthu ameneyo kuchiritsa anthu. Imeneyo ndi mphatso ya machiritso. Mulungu akhoza kusunthira pa inu kupyolera mu mphatso ya machiritso ndipo inu mumaika manja anu pa munthu; ndipo mwinamwache iye akhoza kudwala mwakayakaya ndi kuchiritsidwa nthawi yomweyo; ndipo mwina inu simunapemphererepo anthu ambiri ndi kuwaona iwo akuchiritsidwa, koma Mulungu anakuonetserani inu chifundo nthawi iyi. Imeneyo ndi mphatso ya machiritso.

Ndi chimene Mulungu ali nacho ku Mpingo. Mukuona, ngati inu muli ndi Mzimu Woyera inu muli okhoza kukhala nazo izi zonse. Ngati muli naye Yesu Khristu, mphatso izi zonse ziri mwa Khristu ndipo Iye akufuna kugwiritsa ntchito mphatso izi mu Mpingo. Taonani ichi, taonani m'mene Paulo anaziikira izi apa. Iye anabweretsa umodzi wa Mzimu ndi m'mene aliri Ambuye m'modzi, chikhulupiriro chimodzi, ndi m'mene tingachitire; ndiye kenako anationetsera m'mene zikanabwerera. Iye anati, "Pamene Iye anakwera kumwamba, Iye anapereka mphatso kwa anthu. Choyamba atumwi, kachiwiri aneneri ..." Ndipo anati, "Izi ndi zofikitsa oyeramtima ku ungwiro, ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu, mpakana tonse tikafike ku umodzi wa chikhulupiriro; kuti tisakhalenso makanda kugwedezeka uku ndi uko." Ndiye <u>*kenako*</u>, ndi <u>*kenako*</u>, iye akuti, Vesi 15- ***"Koma ndi kuchita zoona mwa chikondi tikakule mu zinthu zonse, kufikira Iye amene ali mutu ndiye Khristu; Kuchokera mwa Iye thupi lonse*** (iye sakulankhula za utumiki) ***lokowanidwa ndi kulumikizidwa pamodzi*** (kulumikizidwa -ndiko kuphathikana) ***pothandizana mfundo yonse, monga mwa kuchititsa kwa <u>chiwalo chonse</u> pa muyeso wache,*** (gawo lirilonse, mukuona, osangoti utumiki okha), ***lichita makulidwe a thupi, kufikira chimango chache mwa chikondi."*** Ndi pamene wina amangiriza mzache. Mwina m'bale uyu kapena mlongo alankhula zina kapena kuchita zina kumangiriza m'bale wina kapena mlongo. Nthawi zambiri zimandimangirira ine kungokuonani inu mukubwera ku malo a tchalitchi kudzasonkhana. Mulungu akuika thupi palimodzi.

Chabwino, tiyeni tionenso m'mene tadutsamo- "Umodzi Kupyolera mu Utsogoleri," kukhala mutu wa uthenga. Utsogoleri umene umabweretsa umodzi ndi utumiki usanu kuyambira 'oyamba atumwi.' Utsogoleri ukangobwera ndipo Mulungu ndikutenga utumiki usanu kugwira ntchito, kenako iwo ali wofikitsa oyeramtima ku ungwiro, kukulamsinkhu, kumangirira. *"Kufikitsa oyeramtima ku ungwiro, ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu."* Kenako, mukuona, ife tikukula mu uthunthu wangwiro, ndipo sitirinso ogwedezekagwedezeka uku ndi uko, ndipo tikulankhula zoona mwa chikondi. Umu ndi m'mene Paulo wazilembera. Kenako, iye akuti, thupi lonse limayamba kudzimangirira lokha, mbali iliyonse. Iye akuti mbali iliyonse ya thupi imayamba kuchita chinthu chake; chifukwa utumiki wapanga dongosolo la kulingalira kwawo iwo sakuyenera kuvutika ndi kumadandaura, "Kodi tikulondora mu chiphunzitso? Kodi mpingo uwu ukulondora? Kodi gulu ilo likulondora? Kodi mlaliki uyu akulondora?" Mukuona, inu mukamavutika choncho Mulungu sangakudalitseni ndi kukutsogolerani. Inu mukamvetsa, "Hey, izi ndi zoona; ine ndikumva bwino ndi izo; ine ndikudziwa kuti ndi za Mulungu, ine ndikudziwa kuti ndi zoona." Kotero inu mukhoza kuyamba kumalingira pa Mulungu, "Ambuye, mundigwiritse ntchito kudalitsa ana anu." Ndi angati amene amapemphera choncho pamene abwera ku tchalitchi? "Ambuye, kodi mungagwiritseko ntchito mphatso mu moyo wanga kudalitsa winawake?" Mukuona, gawo lirilonse limamangiriza ndi kudalitsa limzache.

Mukuona, M'bale Clifford anachitira umboni za zimitanda. Iye anali ndi maloto asanapite ku ntchito kuti kunali mitanda mu msewu pa malo pena pake. Iye anakumbukira maloto amenewo ali mu njira akupita ku ntchito ndiye amayang'ana izo, kuyembekezera izo, ndiye zinali monga maloto analankhulira. Mukuona, izi zinandimangirira ine ndikundikweza. Zinandipanga ine kudziwa, "Hey Mulungu akusuntha. Mulungu akusuntha ndi anthu ake." Ndi chimene inu mukufuna kuchita, kuchitira umboni wa zinthu izi Mulungu wachita kwa

inu; kuwauza oyeramtima ena, chifukwa zimatirimbikitsa ife. Pamene mukhala ndipo zikuchitika inu mumafuna kuchitira umboni za izo. Zimathandiza anthu ena, zimathandiza chikhulupiriro chawo kukwera. Paulo anati, “Chikhulupiriro chanu chimakula mochuluka.”

Ine ndikunyadira inu. Ine ndikukhulupirira kuti muli munjira yolondora. Ine ndikukhulupirira kuti mukuyenda njira yolondora, koma ine ndikukhulupirira kuti tiri nawo mwai wopitirira. Ine ndikukhulupirira kuti m’mitima mwathu ife tikhoza kupeza malo mu mzimu wathu ndi mu moyo wathu kuti mukhale malingaliro a mtundu uwu: “Ambuye ndingachite chiyani kuti ndikhale m’daslitso kwa ana anu ena?” Zikhoza kungoyenda ndi kugwirana manja ndi wina aliyense ndi kuwauza iwo mukunyadira iwo; zinthu monga choncho. Chabwino, Ambuye akudalitseni. Ine ndikumverera ndalankhula chimene Ambuye akanati ndilankhule madzulo ano. Ine ndikunyadira inu. Ine ndikunyadira zimene inu mukuchita chifukwa cha uthenga. Opanda inu komanso thandizo lanu sitikanatha kutengera uthenga uwu kunja. Ine ndimakukondani mwa Ambuye. Ambuye akudalitseni pamene mukulingalira pa Iye ndi kukula mu chisomo chake ndi mu chidziwitso chake.

Atate Wakumwamba, mu dzina lanu Yesu Khristu, tikubwera kwa inu kukuyamikani chifukwa cha chifundo ndi ubwino wanu, kukuthokozani Ambuye, chifukwa muli yemweyo dzulo, lero, ndi kunthawi zosatha. Tengani mau awa ndipo muwagwiritse iwo ku ulemerero wanu tikupemphera, ndipo tidzakhala osamalitsa kukuyamikani mu dzina lodabwitsa la Yesu Khristu. Amen